Chidziwitso cha Matenda a Mthomba ya Nkhuku (Chikwirikwiti)

Matenda awa amapezeka kwambiri muno m'Malawi. Ndipo amafala kuchokera ku nkhuku zodwala pamene zakhudzana ndi zamoyo.

Photo: Trufosa Phiri
(Facebook - Local Chicken Farmers in Malawi)

Maonekedwe a Matendawa

- Zizindikiro: Tizilonda totupa pa lipombo ndi m'matende. Nthawi zina timaoneka pali ponse pa mutu.
- Nkhuku imadwala matendawa kwa sabata limodzi, nkhuku zina zitha kufa ndi matendawa.

Choyambitsa

- Kachirombo kamtundu wa virus kamene kamapezeka kwambiri muno m'Malawi.

Kuchiza

- Palibe mankhwala ochiza matendawa. Ngati matenda agwa m'khola, amatha okha.
- Koma kupaka mankhwala a iodine pa tizilonda kumathandiza kuchira.

Kuteteza

- Kuli katemera amene amapezeka ku veterinary shops. Katemerayu amateteza matendawa ngati sanagwa m'khola.

Copyright © 2013-2020 Rural Poultry Centre - All rights reserved
Copyright and linking policy «» Privacy policy «» Terms and conditions «» FAQ
Site last reviewed 30 December 2021